# UTHENGA WAPADERA WOCHOKERA KWA WA PAMPANDO WA BUNGWE LOYENDETSA ZISANKHO WOKHUDZA NDONDOMEKO YA KAPONYEDWE KA VOTI PA CHISANKHO CHAPADERA CHA PA 30 JUNE 2026.

Moni amayi ndi abambo, anyamata ndi asungwana

M'malo mwa Bungwe loyendetsa zisankho, lero ndabwera ndi uthenga wokhudza kuponya voti pa chisankho chapadera chomwe chichitike lachiwiri pa 30 June 2026 ku madera atatu a phungu a Nyumba ya Malamulo komanso awiri a makhansala motere:

**Madera a Phungu:**

1. Lilongwe City Bwaila;
2. Balaka Mulunguzi ndi
3. Machinga Mikoko.

**Komanso ku ma wodi awa:-**

1. Uliwa Ward ku Karonga South Constituency
2. Kanjuli Ward ku Machinga Central East Constituency

Ndondomeko zake zonse zili motere:

**Oyenera kuponya voti ndani?**

Pa Chisankho chimenechi woyenera kuponya voti ndi anthu awa:

- Onse amene analembetsa mu kaundula wa chisankho chachikulu cha 2025 ku madera amene kuli chisankho chapadera
- Onse amene analembetsa mu kaundula wa chisankho pokonzekera chisankho chapaderachi, kuchokera pa 12 May mpaka pa 18 May chaka chino.

Popita kukaponya voti, kumbukirani kutenga chiphaso chanu chovotera. Ngati chinatayika, kusowa kapena mwanjira ina iri yonse simukuchiona, pitanibe kumalo omwe munalembetsera ndipo wogwira ntchito ya chisankho akayang'ana dzina lanu mu kaundula wa chisankho. Dzina lanu likakapezeka akakulolani kuti muponye voti.

**Nthawi ndi ndondomeko yoponyera voti**

Monga momwe malamulo a Chisankho amanenera, nthawi yoponyera voti ndi kuyambira 6 koloko m'mawa mpaka 4 koloko masana. Kwa amene 4 koloko idzawakwanire ali pamzere iwowo adzaloledwa kuponya voti. Koma amene adzabwere folo koloko itakwana kale, sadzaloledwa kuponya voti ngakhale pamalopo pali nzere wa anthu oponya voti.

Bungwe loyendetsa chisankho likukumbutsa anthu onse kuti, popita kukavota ndikoletsedwa kuvala, kunyamula kapena kupachika makaka aliwonse a chipani kapena a wopikisana nawo pa chisankho moyima pawokha. Amene adzapite kumalo woponyera voti atavala za chipani kapena za wopikisana nawo moyima payekha adzabwezedwa kuti akasinthe ndi kubweranso kudzavota bwino. Mkulu woyang'anira malo woponyera voti wapatsidwanso mphamvu yochotsa makaka a chipani ngati eni ake sanachotse wokha pa malo woponyera voti.

Mukafika pa malo woponyera voti, chonde kawonetsetseni kuti mwayima pamzere wolondola malingana ndi dzina la abambo anu. Ngati pali chikayiko, afunseni oyendetsa chisankho kuti akuuzeni

mzere umene muyenera kuyima. Mukhozanso kuyimba *2509# kuti mudziwe mzere umene mukuyenera kuyima povota.

Mukakafika pa tebulo loyamba akayamba kaye atsimikizira kuti dzina lanu ngati lirimo mu kaundula wa chisankho. Chonde dziwani kuti kutsimikizira mayina mu kaundula wa chisankho kukayamba ndi kuyika chala chanu pa makina amene akaonetse nkhope, dzina lanu ndi komwe munalembetsera voti. Mukatero dzina lanu akalitsimikiziranso mu kaundula wa pepala amene akapezekenso pa malo woponyera voti. Dziwaninso kuti ma monitala omwe akapezeke pamalo woponyera voti, nawonso akakhala ndi kaundula wa pepala kuti nawonso azikalembera kuti atsimikizira anthu amene akudzaponya voti patsikulo.

Akakatsimikiza dzina lanu mu kaundula, mudzapita pa tebulo lachiwiri pamene mukanyike chala chanu cha mkombaphala chakumanja mu inki. Chonde dziwani kuti inki imeneyi siyowopsya ku umoyo wa munthu, choncho musakavutike kukayichotsa mukapita kunyumba, imachoka yokha ndi nthawi.

Mukanyika chala mu ink, mukapatsidwa pepala lovotela ndipo mukapita pa kanyumba komata kuti mukasankhe amene mukufuna pochonga Kapena kudinda mu kabokosi ka kumapeto kwa mzere womwe dzina lawo liri. Kenako mukapinda pepalalo bwinobwino, katatu kapena kuposera apo, kuwonetsetsa kuti kumene mwavotera kuli mkati, ndi kukaponya pepalalo mu bokosi loponyera voti, lomwe likayikidwe pamalo owonekera kwa aliyense. Mukatero mwamaliza kuponya voti.

Monga mwa dongosolo lake, aliyense akakamaliza kuvota, akuyenera kupita kwawo kukadikira zotsatira. Sizovomelezeka kuti anthu adzikhalabe pa malo woponyera voti. Wokhawo amene avomerezedwa ngati nthumwi za wopikisana pa chisankho komanso woyimilira mabungwe omwe siaboma amene adzavomerezedwe ndi bungwe loyendetsa chisankho ndi amene akuyenera kukhala pa malo woponyera voti.

Dziwaninso kuti ndikulakwira malamulo kuwulula munthu amene mukufuna kumuvotera kapena mwamuvotera pamene mukanali pa malo woponyera voti chifukwa voti yanu ndi yachinsinsi, komanso khalidwe limeneli likhoza kuchititsa kuti pamalo a chisankho payambike maphokoso. Mukakhala pa malo woponyera voti simukuyeneranso kuwonetsa kapena kupanga zizindikiro zowonetsa chipani chimene mumachikonda kapena wopikisana nawo pa chisankho amene mumamukonda.

Dziwaninso kuti ndikuphwanya lamulo kuwumiriza kapena kunyengerera munthu kuti awulule munthu amene wamuvotera. Aliyense akupemphedwa kuti adziwe za lamulo limeneli.

## Kaponyedwe ka voti kwa anthu amene ali ndi ulumali

Anthu onse aulumali adzathandizidwa mwachangu ndipo sakuyenera kuyima nawo pa mzere. Anthuwa akafika pamalo woponyera voti akuyenera akadzionetsele kwa woyendetsa

chisankho amene adzawathandize kukawakhazika kutsogolo kwa mzere.

Chimodzimodzinso kwa amayi woyembekezera, anthu okalamba ndi odwala, onse adzathandizidwa msanga. Kwa anthu wolumala amene amayenda panjinga (wheelchair) asade nkhawa popeza adzathandizidwa kuti aponye voti popanda kutsika pa njinga yawo.

Kwa aulumali m'njira zosiyanasiyana monga kumva kapena kupenya: lamulo likuti anthu woterewo adzabwere ndi munthu amene akumukhulupirira komanso akhale wakuti munthuyo analembetsa nkaundula wa voti. Munthu ameneyu ndi amene adzawathandize kuponya voti. Ngati sabwera ndi munthu owathandiza, lamulo limanena kuti: oyendetsa chisankho pa malopo atha kumuthandiza munthu woteroyo payekha.

Pamenepa ndikupempha mamonitala kuti adzathe kumvetsetsa ndi kutsatira zimene lamulo limanena. Nthawi zina pamakhala kusamvetsetsa chifukwa ma monitala amafuna kuti akaone nawo kuti akumusankhira molondola kapena ayi. Izi zimachotsa chinsinsi chavoti ndipo ndizoletsedwa ndi malamulo.

Komanso dziwani kuti bungwe loyendetsa zisankho lapanga chikombole chomwe chidzathandize kuti anthu amene ali ndi vuto lopenya kuti akavote wosathandizidwa ndi munthu wina. Pogwiritsa nchito chikombole chimenechi anthu amenewa adzatha kusankha kandideti wakumtima kwawo pogwiritsa ntchito zala zawo. Anthu awa akadzafika polandira pepala lovotera, ogwira ntchito ya

chisankho adzawapatsanso chikombole chimenechi ndi kuwafotokozera m'mene angakagwiritsire ntchito.

## Ngati chiphaso cha voti chatayika kapena kuwonongeka

Aliyense wokavota akupemphedwa kuti adzakumbukire kunyamula chiphaso chovotera. Kwa amene adataya ziphaso zawo, kaya zinabedwa, kuwonongeka, kapena kulandidwa, ali wololedwa kuponya voti ku malo amene adalembetsera mayina awo mu kaundula wa chisankho, ngati atatsimikizidwa kuti analembetsadi pamalopo.

Anthu woterewa akakafika pamalo wovotera ayenera kukadziwitsa woyendetsa chisankho kuti anataya chiphaso chawo. Pamenepo dzina lawo lidzafufuzidwa mu kaundula wa chisankho ndipo likapezeka adzaloledwa kuvota. Ngati munthu obwera wopanda chiphaso cha voti ndipo dzina lawo silikupezeka mu kaundula wa voti, iwowa sadzaloledwa kuponya voti chifukwa umboni owonetsa kuti analembetsa voti palibepo.

## Kachongedwe kolondola povota

Ngati bungwe tayetsetsa kuphunzitsa anthu m'mene angasankhile munthu amene akumufuna molondola. Dziwani kuti kusankha kolondola ndi kuchonga kapena kudinda mkati mwa bokosi limodzi basi. Chonde dziwani kuti voti imakhala yosawerengedwa ngati ingakhale ndi chimodzi mwa izi:

I. Kukhala yosachonga kapena kudinda malo alionse

II. Ngati pepala lovotela lang'ambika ndi kukhala zidutswa ziwiri kapena kuposera.

III. Ngati pepala lovotela lachongedwa malo oposa amodzi

IV. Ngati pepala lovotela lapakika ndi inki malo wosiyanasiyana;

V. Ngati pepala lovotela, lalembedwa ziri zonse, kaya zokomera kapenanso zoyipira wopikisana wina aliyense kapenanso bungwe, angakhalenso munthu wina ali yense;

VI. Ngati pepala lovotera lalembedwa dzina, signature, kapena chizindikiro chiri chonse chomwe chingaganiziridwe kuti ndi dzina kapena signature ya munthu;

VII. Ngati pepala lovotela lapezeka ndi mawu aliwonse wothokoza kapena a chipongwe;

Ngati china mwa zinthu izi zitachitika, zidzapangitsa kuti voti ikhale yosavomerezeka zomwe zingachepetse mwai wa munthu kupambana pa Chisankho.

Choncho ndipemphe onse amene akukaponya voti kuti apewe zimene zingapangitse voti yao kuti isakawerengedwe chifukwa zimenezo zikhoza kupangitsa unthu amene amafuna kuvotera kuti alephere pa chisankho.

**Udindo wa mamonitala pa nthawi yoponya voti**

Zipani zonse zomwe zikupikisana nawo komanso iwo amene akuyima pawokha, ndiwololedwa kuika ma monitala, awiri pa mzere uli onse

woponyera voti. Ndipo mamonitala amenewa akupemphwedwa kukafika pa malo woponyera voti nthawi ya 5 koloko m'mawa.

Pa nthawi yonse imene azidzagwira ntchito yawo pamalo woponyela voti, iwo akuyenera kuvala chizindikiro cha ntchito yawoyi chimene Komishoni idzawapatse, ndi cholinga chakuti azidzazindikiridwa mwachangu.

Pogwira ntchito yawo, woyimira zipani ali ndi ma ufulu ndi maudindo awa:

- Kuwonetsetsa ndi kutsimikizira kuponya voti kusanayembe, kuti mu bokosi lovotera mulibemo chiri chonse;
- Kuonetsetsa pogwiritsa ntchito kaundula wa voti wapepala kuti amene akuvota ndi anthudi woyenera kuvota pamalopo;
- Kuwonerera m'mene ndondomeko zonse za chisankho zikuyendera pa malo woponyela voti, powonetsetsa kuti malamulo akutsatidwa bwinobwino ndipo palibe zachinyengo ziri zonse zomwe zikuchitika;
- Kukhalapo pamalo a chisankho nthawi yonse kuti athe kuona zonse zochitika zokhudzana ndi kuponya komanso kuwerengera mavoti.
- Kufunsa woyendetsa chisankho kuti awafotokozere m'mene zinthu zikuyendera pa malo woponyela voti ngati pali chikaiko.

- Kuwonetsetsa pamene akuwerengera mavoti kwayamba, kuti mavoti onse atulutsidwamo mu ballot box ndipo kuti mulibe otsalamo.

- Kulemba ndi kupereka ku komishoni zidandaulo zomwe zingakhale kuti sanakhutitsidwe nazo ndi m'mene mkulu wachisankho pamalo woponyera voti walongosolela;

- Kusayinira mapepala a zotsatira pa malo woponyera voti pamene akugwirapo ntchito;

- Kulandira zotsatira za Chisankho za pamalo woponyera voti pamene agwira ntchito

Tonse tiyenera kukumbukira ndi kuwonetsetsa kuti Monitala:

- Sakuyenera kusokoneza ntchito yoponya kapena kuwerengera mavoti;
- Sakuyenera kuona kuti anthu amene akuponya voti akusankha ndani, popeza voti ndi ya chinsinsi;
- Sakuyenera kuvala makaka a chipani chiri chonse;
- Sakuyenera kulankhulitsana kapena kuwathandizila anthu amene abwera kudzaponya voti;

- Sakuyenera kupanga kampeni, kuwafunsa wodzaponya voti kuti avotera ndani komanso kuwanyengerera kuti avotere m'modzi wa wopikisana nawo.

Mwapaderadera, ndibwereze kukumbutsa ma monitala kuti ali ndi ufulu wopereka dandaulo lolemba kwa woyendetsa chisankho pa

malo oponyela voti ngati sakukhutitsidwa ndi chiri chonse chokhuza m'mene ntchito yachisankho ikuyendera pa malo woponyera voti (polling station). Ndipo woyendetsa chisankho alibe mphamvu zokana kulandira dandaulo limenelo.

**Kuwerenga mavoti**

Kuwerengera mavoti kudzayamba nthawi imene kuponya voti kwatha. Kumbukirani kuti malo woponyera voti adzatsekedwa 4 koloko masana. Palibe bokosi loponyera voti limene lidzachoke pa malopo, mavoti asanawerengedwe. Woyendetsa chisankho pa malowo ndi anthu wokhawo amene adzaloledwe kuwerengera mavoti, woyimilira zipani ndi wopikisana nawo adzakhalepo panthawiyi kuti adzaonenerere kuwerenga kwa mavotiko.

Dziwani kuti mzere uli wonse (Polling Station) udzawerenga mavoti pawokha. Pomaliza kuwerengera ndikulemba zotsatirazo, woyimilira makandideti onse akuyenera kudzasainira nawo pa zipepala zomwe zikuwonetsa zotsatirazo. Kudzatha kusainiraku, azipani ndi onse woyimilira wopikisana adzapatsidwa mpata wotola chithunzi cha zotsatirazo, kuti asunge komanso kutumiza komwe iwo angafune kutero. Kuwonjezera apo, ma monitala onse adzapatsidwa zotsatira za Chisankho zosayinidwa, ndipo zotsatirazo zidzakhomedwanso pamalo a chisankhowo kuti anthu ena athe kuwona nawo. Potsiriza mkulu woyendetsa chisankho pa mzere umenewo adzanyamula zotsatira za pamzere wake ndi kukapereka ku Constituency Tally Centre.

Bungwe loyendetsa chisankho likuyembekeza kuti lidzalengeza zotsatira za chisankho chapaderachi pa 3 July 2026.

**Pempho la bata ndi mtendere**

Ndikupempheni a Malawi anzanga kuti tisunge bata ndi mtendere munthawi yonse imene anthu akhale akuponya voti mpaka pomwe mavoti adzakhale akuwerengedwa komanso zotsatira zidzakhale zikulengezedwa. Ngati mungakhale ndi dandaulo liri lonse lokhudza chisankho, chonde kalipelekeni kwa mkulu woyendetsa chisankho pa malo a voti pamene chomwe mukudandaulacho chachitika.

Mulungu akudalitseni pomwe mukukaponya voti yanu lachiwiri lino pa 30 June, 2026. Kumbukirani kuti malo woponyera voti akatsegula 6 koloko m'mawa ndi kutseka 4 koloko masana.

Mulungu akudalitseni,

Komanso adalitse dziko lathu la Malawi,

ZIKOMO KWAMBIRI.